

Uzimu Weniweni - Zolembedwa mu Chichewa

Gawo 5: Mmene Tingakumanirane ndi mudzi weniweni

Zolembedwa ndi Chip Ingram

Kodi munayamba mwadabwapo kuti ndi chifukwa chiyani Akhristu ambiri amakhala kakasi mu uzimu? Baibulo ndi lomveka bwino kwambiri. Limati, “Ngati mwamuna aliyense kapena mayi aliyense ali mwa Khristu, zinthu zakale zapita; onani, zinthu zonse zakhala zatsopano. Komabe, mumakumana ndi anthu aubwino, owonadi, sindikunena akugwa – ndikutanthauza anthu amene amakondadi Mulungu. Amene anawona kusandulizidwa mmadera ambirimbi, ndipo ngakhalenso mu Baibulo nthawi zonse amapezeka, ndipo amafunitsitsa kukula, ndipobe amakhala kuti agunda khoma kapena kuchedwa.

Pali madera ena monga kukwiya kumene sikuoneka ngati kukukhala pansi pa utsogoleri wa Mzimu, kapena mmene mmatchulira zinthu zina kapena mmene amaweruzira anthu ena kapena pali kamoyo kanseri ka madyedwe oyipa pano, mwina chizolowezi chovuta kusiya, ngakhalenso pa internet. Ndiye kenako amadzimva kulakwa kwambiri, ndipo amalondeza Mulungu ndipo amadziperekanso moyo wawo kokwanira ka 25 ndiye kenako amangomva kuti ali kakasi.

Pamenepo ndi pamene Andy anali mmene anabwera kudzayankhula ndi ine, kupatula apo sindikadalota kuti Andy anali kakasi. Andy anabwera pamene ndinali mbusa wa mpingo wina zaka zambirimbi zapitazo. Ndipo ndinakumana naye, ndipo mphindi 10 - 20 zoyambirirazo ndinaganiza, Eeeh, Timakuladi pa nthawiyo, ndipo timafunitsitsa atsogoleri ndipo iye anasamuka kuchokamo ku tawuni.

Ndipo ndinakumana naye, ndinakumana ndi mkazi wake, kungofuna kudziwana, ndipo kunali ngati eeeh, ali ndi mtima wofuna Mulungu. Ndinadzuka mmawa, ndi kukhala ndi nthawi ndi Mulungu. Ndinawona banja lake. Iye anali atakhala Mkhristu kwa nthawi yayitali, kotero ali ndi maudindo atsogoleri ndiponso mmpingo. Ndipo Andy anali munthu wabwino kwambiri, wosangalala ndi wosamalira. Ndipo sindikanalota mkomwe kuti panali kathumba kakang’ono. Kathumba kakang’ono mmoyo mwa Andy kamene kanali kakasi.

Ndipo anandifunsa ngati kuli kotheka kuti tikamwe khofi, ndipo anali ndi china chake chimene anafunitsitsa kugawana nane. Ndinati “Chabwino, Andy, ndikondwera kutero.” Ndipo tinakhala pansi ndipo anayamba kundiwuza za kachipinda kameneko, kamene kanali kotsekedwa, ndipo anali atayesetsa kwambiri ndipo anali kakasi. Anati, “Ukudziwa, zinayambika pamene mwina ndinali ndi zaka uuuu zisanu ndi zitatu kapena zisanu ndi zinayi ndiye ndinalandira kabuku ka Sears kanabwera pamodzi ndi makalata

ndipo ndimavundukula masamba ake ndipo ndinafika pa gawo la zovala za mkati. Kenako ndiye ndinapeza mabuku ena pansa pa bedi la bambo anga.”

“Pamene ndinali wachinyamata, ndinali nditakhazikika kotheratu mu chizolowezi chokanika kusiya chowonera zolaula. Pomwe internet inachitika, zinali zochuluka kupezeka kwake ndi chinsinsi chimene chinalipo”. Ndipo anati “Chip, ndapemphera, ndasala kudya, ndaloweza ndime zambiri, ndapempha Mulungu. Ndimapita masabata angapo kapena miyezi ingapo, ndi moyo wanga wonse,.. mkazi wanga, ndimamukonda, ndine wodzipereka ndithu kwa iye, kwa ana anga. Ndayesetsa kuchita zonse... koma ndi ichi, ndili kakasi.”

Ndiye kenako anagawana nane, anati “Ndinamva china chake pa wailesi zokhudza gulu ili la anthu, ndipo amakumana.” Ndipo anati, “koma kwa miyezi isanu ndi umodzi yapitayo, ndakhala ndikuyendetsa kwa mphindi 45 pa usiku wa lachinayi ndikukumana ndi gulu ili la anthu ndipo ndinamasulidwa.” Yankho la chifukwa chimene anali kakasi ngakhale panali Mawu a Mulungu ndi zina zonse zinabwera pomwe anakumana ndi gulu ilo. Ndipo ndikuuzeni pang’ono za icho.

Gawo la yankho ndi kuti mbewu yabwino kwambiri mu nthaka yabwino kwambiri siyingamere mmalo olakwika. Mungathe kulemba “Luka mutu 8 kapena Marko mutu 4”, ndime zofanana, ndipo Yesu akukamba zokhudza kuyitana lye mwini, lye ndi wofesa, ndipo chimene amafesa ndi mbewu, ndipo mbewu ndi Mau a Mulungu, ndipo dothi ndi mitima ya anthu, malo osiyanasiyana olandirira amene Mau a Mulungu amalandira.

Ndipo ngati mukudziwa nkhani yonse, zina zili mumsewu, ndipo zina pa padothi la miyala. Ndipo ndi mmene mitima ya anthu osiyanasiyana ilili. Ndipo zina pomwe panali minga ndipo ena ndi nthaka yabwino, mitima yabwino ndi yowona, anthu amene ndi owonadi ndi kufunitsitsa kukula.

Koma pano pali chimene ndikufuna. Mbeu yabwino kwambiri, Mau a Mulungu, munthaka yabwino kwambiri, mtima wabwino ndi woona sangakule pa malo olakwika. Pali zinthu zina mmoyo mwanu ndi mmoyo mwanga, ndi mmoyo mwa okhulupirira aliyense, kusandulika sukungachitike, mosatengera kuti mwakhala mu Baibulo motani, osatengera kuti mwakhala mokhulupirika motani ndi kuti kukhumba kwa mtima kwanu ndi motani kupatula inuyo kukhala pa malo pomwe kungachifikire.

Pali chilengedwe chapaderadera malo amene Mulungu ali nawo amene amabweretsa za kusandulika pomwe mbeu ya mawu a Mulungu mumtima mwanu ndi mwanga alipo. Ndipo ngati pali zinthu zina zimene palibepo, mudzakhala kakasi.

Zindikirani mu zolemba zanu, pang’ono kukhala ndi maziko a Baibulo pano, lamulo la Yesu, likufunikira chilengedwe chapadera kapena malo. Usiku womaliza pa dziko

lapansi lye anasambitsa mapazi awo, ndipo kenako anawatembenukira iwo ndi kuwayang'ana maso ndi maso, ndipo lye anati, “Ndikufuna inu” – ili ndi lamulo latsopano – “mukondane wina ndi mnzache monga momwenso lne ndakondera inu.” Modzipereka nsembe, moona kwenikweni, perekani moyo wanu kwa wina ndi mnzake. Koma pafunika malo.

Chitsanzo chachiwiiri cha Yesu kufuna chilengedwe chapaderadera ndi pomwe lye anafuna kusintha dziko lapansi, lye anayamba ndi kuphunzitsa. Ndipo pomwe lye anaphunzitsa panali chikhamu cha anthu ndipo anapanga zozizwitsa. Koma pomwe lye anafuna kukhala ndi timu yake pamodzi imene idzasinthe dziko lapansi, lye anakhala usiku onse, lye anapemphera usiku onse, ndipo lye anasankha 12, ndime ikutero, “kukhala ndi lye.”

Khamu la anthu anamva choonadi. Khumi ndi awiri anaphunzira kukhala moyo. Panali chilengedwe chimene anachisowekera kukhalamo kuti choonadi chonse chitsikire mmitima yawo ndi mmiyoyo yawo ndi maubale awo.

Kuchita kwa mpingo woyamba ndi zotsatria zake zimatsutsana mu chilengedwe chomwecho. Mukudziwa nkhani yake. Mu Machitidwe Atumwi 2 anadzipereka... Atumwi kuphunzitsa, ndi ku chiyanjano chosonkhana pamodzi, ndi kunyema mkate, ndi ku mgonero wa Ambuye.

Likunena kuti, kenako, anasonkhana bwanji? Mabwalo a mu kachisi ndipo Petro kapena Yohane kapena wina wake amatha kulalikira ndi kuphunzitsa Akhristu onse atsopano, ndipo kenako kuti? Kuchokera nyumba ndi nyumba.

Pomaliza, mbiri ya mpingo – yakale ndi yatsopano imatsimikizira za chilengedwe ichi chapaderadera cha kukula mu uzimu ndi kusandulika. Ndipo kaya ndikubwezeni mmbuyo ku chitsitsimutso cha nthawi ya a Moravian kapena a Wesley kapena a Welsh, ndipo amatha kusonkhanitsa midzi ya anthu pamodzi kapena ndikubwezeni ku Korea kumene kunaliberetu Akhristu, zaka makumi asanu kapena asanu ndi chimodzi zapitazo kuyenda kwa mmagulu kapena kuyenda kwa magulu ang'onoang'ono amene tsopano atekesa dziko lapansi.

Pano pali chimene ndikufuna inu mutenge: Chilengedwe chencheni kapena malo a paderadera amene mbewu ya Mau a Mulungu mumtima mwanu imene ndi ubwino ndi moonadi ndipo ikufuna kukula ndi mudzi wenweni. Ndi mudzi weniweni. Dziwani mtundu umene ukutenga ndilo gulu laling'ono. Gulu likhoza kukhala anthu atatu, anthu anayi, anthu khumi, koma umenewo ndi mtundu chabe, chimene chili chotengera.

Musadzayerekeze, kusokoneza kukhala mu gulu laling'ono lenileni la mudzi. Ndakhalapo mmagulu ang'onoang'ono amene mulibe mudzi weniweni, nanga inu

munakhalapo? Munayamba mwapita ku gulu laling'ono ndipo wina wake watsegula Baibulo ndi kuwerenga pang'ono, mukudziwa, kapena mwina mwake kufunsa mafunso ena kuchokera mu mlozo wa mawerengedwe ndi kunena kuti, "Chabwino, kodi mwapeza chiyani pa funso lachinayi. Kodi mwapeza chiyani pa funso lachisanu ndi chiwiri? Ohoo izi ndi zabwino, ndi zabwino."

Ndiye kenako funso lina lozama lafunsidwa ndipo yankho ndi "Ooh, mwina mwake... mwina mwake ndisanaganizire kwambiri." "Ooh chabwino, zikomo kwambiri pogawana nafe mozama. Kodi pali zofunika kupemphereredwa?" "Eeeh, chiuno changa chikupweteka, chikupweteka kwambiri," mukudziwa? Ndipo kenako mmakhala ngati mwathana nazo, kenako mukuyima ndipo amayi afika pamenepo. "Kodi munamvapo za ichi kapena icho? Kodi mukudziwa chimene chikuchitika apapo?"

Ndipo azibambo ali pano kulankhulana za masewero. Ndiye kenako mmadya tizakudya, ndi kulowa mgalimoto mwanu ndi kunena, "Zinali bwino?" Chabwino zinali bwino, koma simunatchule kuti ndi mudzi weniweni. Ndi chiyambi chabwino. Ndi kulumikizana. Musadeweze mwadziwako anthu ena.

Koma mudzi weniweni ndi ozama. Mudzi weniweni ndi chilengedwe ichi pomwe anthu amapereka miyoyo yawo kwa wina ndi mnzake. Mudzi weniweni ndi umene mumatenga gulu la anthu ndi kunena kuti, "Mukudziwa inu chiyani, ife tisintha dziko lapansi," ndipo iwo anali monga chomwecho pozungulira Yesu. Mudzi weniweni ndi kukhala pansu pa chisautso ndi kumva Mau a Mulungu ndi kupita ku nyumba ndi nyumba kuthandizana wina ndi mnzake kukhala moyo umenewewo.

Pamenepo chikudzutsa mafunso awiri ofunikira kwambiri. Funso loyamba ndi: Kodi mudzi weniweni ndi chiyani? Ndiye kenako lachiwiri ndi: Kodi mmapeza bwanji? Ndipo yankho ku mafunso onse awiri lili mu Aroma mutu 12 ndime 9 mpaka 13. Ndipo mundime 1, tikupunzira kuti chenicheni chimene Mulungu amafuna kuchokera kwa ife tonse ndi chiyani? Iye amafuna ife kugonjera kwa Iye, zonse zimene ife tili, zonse zimene tili nazo. Mudime 2, tinanena kuti pali mdani wa moyo wathu. Pali mayendetsedwe a dziko lapansi amene akuyesetsa kunyenga mtima wathu kuchoka kwa Mpulumutsi wathu. Ndipo "sitiyenera kufaniziridwa ndi za dziko lapansi koma kusandulizidwa ndi kukonzedwanso kwa mitima yathu," kukhala opatulika kuchokamo mu zinthu zopindula za dziko lapansi.

Mukukumana kwathu komaliza timayang'ana ndime 3 mpaka 8, ndipo tinaphunzira kuti tisaganizire mokwera kwambiri kapena motsika kwambiri, koma kukhala ndikudziyesa kodekha, kudziwa kumene tikukwanira mu thupi. Ndipo tsopano chimene ayankhule ndi chokhudza kutumikira mu chikondi. Iye adzayankhula zokhudza za mtundu wa maubale amene tiyenera kukhala nawo monga ngati okhulupirira anzathu. Mu ndime 9

mudzaowona kuti mudzi weniweni ndi “inu enieni” kudziwonetsera. Ndime 10 idzanena kuti “inu weniweni” mukusowekera kukumaa ndi zosowa zenizeni. Ndiye kenako mu ndime 11, adzanena kuti “inu weniweni” akusowekera kukumana ndi zosowa zenizeni koma pa chifukwa cholondola. Ndipo mu ndime 12 ndi 13, “inu weniweni” akusowekera kukumana ndi zosowekera zenizeni pa chifukwa cholondola ndi kuchichita icho mu njira yolondola.

Kwa ena mwa inu, muli pamene mnzanga Andy anali. Mumakonda Mulungu, muli ndi mtima wabwino, mukugwiritsa ntchito mawu a Mulungu, koma muli kakasi. Pali khoma. Muli ndi mtima wokwiya kwambiri ndipo mumamva kuwawa zokhudza mkwiyo. Muli ndi zinthu mmoyo mwanu zimene mukudziwa kuti simuzifuna ndipo mwamuwuza Mulungu “pepani” ndi mukufuna kusintha ndipo mwayesetsa kwambiri kusintha, simukuwonabe kusandulika kuli konse.

Ndikukuwuzani inu, mphindi iyi pa tsiku la lero mwina ndi yankho la Mulungu ku zachilngedwe chimene zina mwa zinthuzo zimene mwakhala mukulimbana nazo kwa nthawi yayitali lye angathe kuzisintha. Koma sikuchitika pakokha. Koterotiyeni tiwonere limodzi, Kodi mudzi weniweni ndi chyani, ndipo mwina mwake chofunikira kwambiri, mungapeze bwanji?

Choyamba kuchokera pa ndime 9, mudzi wenweni ndi “inu eni” osati chinthunthunzi cha inu eni ake. Sabata latha tinakamba za kudziyesa inu eni ake modekha ndi mmene anthu ambiri timanyengezera kukhala chimene tikufuna anthu aganizire za ife.

Simungathe kukhala ndi mudzi weniweni pokhapokha inu weniweni” awonetsedwe. Akunena kuti, “Chikondano chikhale chopanda chinyengo. Dana nacho choipa; gwirizana nacho chabwino.” Makhalidwe awiri a “inu enieni” awonekera apa, choyamba ,weniweni, ndi lachiwiri, ndi chiyero. Pomwe Mau akunena kuti, “Chikondano chikhale chopanda chinyengo” Zungulizani mawu akuti “chopanda chinyengo” ndi pamwamba pake mulembe “chinyengo.”

Paulo akubwerekera ku chilankhulo cha chiGreek cha mu nthawi yake ndi mmabwalo a chiGreek a tsiku limenelo, onse ochita nawo zisudzo anali amuna. Ndipo koterotiyeni ngati unali wochita bwino kuzisudzo umatha kutulutsa mawu ako ndi kutenga gawo la amuna, la akazi, nkhalamba, mwana. Ndiye amavala zovala zosiyanasiyana ndipo kenako pamakhala chigoba chimene umatha kuvala.

Ndipo Paulo akutenga mawu a chigoba, ndipo lye akuti “Lolani chikondi chikhale chopanda chigoba, chopanda chinyengo.” Lolani “inu weniweni” kuwonekera. Inde, mukusowekera kukhala wozindikira ndipo mukusowokera kukhala osamala kwa amene mukugawana naye “inu weniweni” koma akunena kuti mudzi weniweni sikungokhala

mu gulu laling'ono. Ndi pomwe inu weniweni amawonekera ndipo mumalola anthu kuwona kuti inu ndinu ndani, potukula, pa nzeru, pozindikira.

Pamenepo lembani mu zolembe zanu ngati mungathe, “Machitidwe Atumwi mutu 5.” Ichi ndi chofunikira kwambiri. Ichi ndi choposa chofunikira kwambiri. Anthu ena mmoyo wawo wonse wa Chikhristu sanakumanepo ndi ichi, ndipo sanapeze chifukwa chake sanakumanepo ndi mphamvu yakusandulika imene Mulungu anatilonjeza mu Malemba.

Tsopano sindinakule monga Mkhristu, sindinastegulepo Baibulo mpaka nditafika zaka 18. Ndiye kotero ulendo wanga wa mu Chipangano Chatsopano unali monga ‘ooh Yaaah’ ndikutanthauza zenizeni Kunali ngati Mateyu, Marko, Luka, Yohane sindinadziwe nkomwe maina a zinthu. Ndiye kenako ndinafika ku Machitidwe Atumwi ndipo ndinazindikira chabwino iyi inali mbiri yoyamba ya Mpingo. Ndiye Yesu anakwera, iye anapita kumwamba, ndipo mu mutu 2, Mpingo unabadwa, ndi mutu 3, iye ndi Yohane akupanga zozizwa. Ndiipo ndi zinthu zopatsa chidwi.

Ndiye kenako mukufika mu mutu 5, ndipo Mpingo ukukula kwambiri ndiye kotero kuli izi zonse zosowekera. Ndikutanthauza makumi a zikwi za anthu tsopano ali mu Mpingo mu kanthawi kochepe. Ndiipo pafupifupi anthu makumi asanu ndi atatu a zana lililonse ndi akapolo, ndipo anthu ochepe, anthu olemera ndi otchuka, ena ndi anthu a kunyumba kwa Herodi ndi ena.

Ndiipo anachita ichi, mu nthawi ya zinthu zadzidzi, onse anabwera pamodzi ndipo anati, “Tikusowekera kuthandizana wina ndi mnzake. Tikusowekera kudzikhutula kwa wina ndi mnzache.

Ndiipo nkhani ikupitilira mu Machitsae Atumwi mutu 5. Lemban

Ndiye kotero mu mutu 4 ukupereka chitsanzo cha mwamuna amene anali wolemera kwambiri amene anali ndi malo mu Cypress pa Chilumba, amene unali wofanana ndi tawuni ngati San Francisco kapena Manhattan, mu mmasiku amenewo. Ndiye kotero anawagulitsa ndi kutenga ndalama, ndi kunena, “Inu tengani izi kuti mukumane ndi chosowokera cha anthu a mu mpingo. Akumva kuwawa kwenikweni.

Ndiipo ndikukhulupirira kuti kunamveka phokoso mu mpingo, ooh, kunali kudzipereka nsembe, kunali kukoma mtima. Ndiipo anthu kunali “Mnyamata, ndikuganizira kuti ichi ndi chimene chikutanthauza kukonda wina ndi mnzake.” Ndiipo dzina lake anali Barnabas. Ndiipo ndikuganiza kuti Barnabas anapeza mbiri yabwino iyi chifukwa anayamba kumutchula iye kuti “Mwana wa chilimbikitso”

i izi chifukwa mutu wanu usanagwere pa msamiro, mukuyenera kuwerenga siyayitali kwambiri. Ndi yopatsa chidwi. Koma ndine Mkhristu watsopano ndiye ndikuwerenga

ichi. Kotero pali banja ili lachichepere. Ndikungoganizira kuti anali achichepere. Mwina mwake sanali achichepere. Ananiasi ndi Safira. Ndiye kotero anayang'anayang'ana mozungulira naganiza, oooh,- aliynse akukamba za Barnabas. Tikulakalaka anthu adzakamba za ife monga ngati akukambira za iye. Tikutsimikiza kuti anthu adzaganizira kuti ndife okoma mtima, okonda ndi wopereka.”

Ndiye kotero anapanga dongosolo. Ndipo dongosolo ndi, pano pali chimene tichite. Tigulitsa gawo ili la munda, ndipo tidzapeza ndalama, ndipo tidzawuza anthu kuti tinagulitsa uwu ndi ndalama izi. Ndipo tazipereka zonse, koma ndalama zina tidzadzisungira tokha, kotero tidzakhala ndi gawo lathu ndi kuzidyanso. Tidzaoneka ngati anthu okoma mtima ndi a chikondi ndi odzipereka nsembe, komanso tidzakhala ndi gawo lalikulu kwambiri la ndalama.

Ndiye kutero, anabwera kudzayankhula ndi Petro, ndipo Mulungu anavumbulutsira Petro chimene chikuchitika. Ndiye Petro akuti “Ananiasi, chifukwa ninji kudzanyenga Mzimu Woyera? Pamene unali nawo, sunali wako kodi? Ndipo pamene unaugulitsa sunali mmanja mwako kodi? Sunakakamizidwe kupereka zambiri kapena zochepa.” Nkhani pano ndi ungwiro, ndipo kenako pompo, phi, anafa. Ndikutanthauza, kugwa kwenikweni kumwalira. Ndipo amuna achichepere anabwera kudzamunyamula. Pa chiyani? Chinyengo chake. Tchimo loyambirira mu Mpingo ndi chinyengo, ndipo chiweruzo chake ndi imfa.

Mkazi wake akubwera patatha maora angapo. Ndipo ndikuganiza kuti Petro akuti, “Ndikutsimikiza kuti sali nawo mu ichi.” Ndiye akunena kuti “Safira, ndi chabwino kukuona iwe. Zinthu zikuyenda bwanji? “Ah zili bwino.” “Ana ali bwanji?” Ndikuwonjezera pang’ono. Ndipo akunena kwa iye, “Kotero, kodi munagulitsa gawo la munda pa mtengo wakuti?” “Eya, mukudziwa, Ananiasi, pomwe wakatiwa ndi munthu wopereka, wokonda, wokoma mtima, wosangalatsa monga ngati amene ine ndili naye, ndipo modzipereka nsembe tapereka zonse...” Aponso ndikuwerenga mkati pakati pa mizere

Ndipo Petro anamuyang’ana iye, ndikuganiza, ndi chisoni mumtima mwake ndipo anati, “Mapazi a anyamata amene anatenga amuna anu adzatenganso inu.” Phi, iye anafa pomwepo. Ndipo akuti mantha akulu anagwa pa mpingo. Inde, mukuseka kapena!

Tsopano, mungoganizira ngati munali musanawerengeko Baibulo ndipo aka ndi koyamba kuwerenga Chipangano Chatsopano ndipo ndinu Mkhristu watsopano, mukuganiza choncho ichi ndi chimene chimachitika kwa anthu a chinyengo? Ndili mmavuto. Ndikutanthauza, mosachotseranso kunali, Ooohh. Pamenepo, ngati Mulungu amachita munjira imeneyi, ndikuganiza kuti amatsindika Mfundo. Onani, ngati

chinyengo chingasakanirepo, chili ngati yisiti ndi buledi chimafikira. Ndipo anthu ngati sali enieni, uthenga wa Yesu ukadakhala utatha mu zaka zochepa.

Ndipo kutero Mulungu amafuna kusonyeza kufunikira kwake ndi kotani pa ichi. Kawirikawii ndinaganiza pamene ndili mbusa, ngati Mulungu atachita izi pa maora 24 mu mpingo wa mu America, tonse a ife tikadatembenukira ku mabaji a abusa athu ndi kukhala mitembo. Mwina mwake ambiri a ife abusa tikadasowekera abusa ena amene akuchita bwino kuposa ife kuti atiyike mmanda.

Koma kodi mukuona? Kodi mukuonadi mpingowo, sunapangidwire gulu la anthu longobwera pamodzi pa zochitika ndi kumva ngati munjira ina amachita china chake chimene chinali cholondola mukhalidwe labwino chifukwa akumvetsera kwa wina wake akukamba za Mulungu, ndipo ngakhalenso kuyimba nyimbo zochepa za kulambira kwa lye, ndiye kenako kulemba ndi kyika mu fayilo, ndi kukhala moyo mnjira yawo ndipo siwolumikizana wina ndi mnzake ndipo ali pa malo otetezeka kumene “inu enieni” mumamaonekera? Ndipo inu mukudziwa chifukwa chimene “inu weniweni” simumawonekra? Chifukwa chomwecho “inu weniweni” sumawonekera mwa ine. Iye akuti, “Chikondano chikhale chopanda chinyengo,” ndiye kenako akuti, “Gwirizana nacho chabwino, dana nacho choipa; Kwenikweni mawuwa ndi “nyansidwa” nacho chimene ndi choipa.

Ndikukumbukira ndi kuwerenga ndi kuphunzira za mawu otchedwa “nyansidwa” ndipo ndi chinthunzi chokhala kunja kwa tawuni kwa kanthawi, ndipo kuti katoni ya mkaka kapena chipatso china, ndiye mukutsegula katoni ya mkaka kununkhiza kuti muwone ngati ndi wabwino. Ndipo fungo lake ndi loyipa kwambiri mwakuti mukufuna kusanza nalo. Kodi munayamba mwapangapo zimenezi? Ilo ndiye mawu akuti “nyansidwa”. Akunena kuti, “nyansidwa ndi choipa” Ambiri mwa ife timadabwa ngati chinthu chathu ndi cholakwa, kapena timayandikira bwanji ku tchimo opanda kugweramo.

Kotero anthu amandifunsa mafunso ngati, “Chabwino kuyika pa mulingo uwu, kapena mulingo uwu mu kanema, mukuganiza kuti ndi zabwino ngati ndingachite ichi?” Kapena, “Inu mukudziwa, panopa tili pa chibwenzi ndipo tikuchita ichi, ichi ndi ichi. Kodi limenelo ndi tchimo logonana kapena tingathe... Kapena “tili ndi ndalama mwakuti ndipo ndikufuna kudziwa kodi ndi zoyamba zosachotsa msonkho kapena zimene achotsa msonkho.... kapena ndingotenga pa gawo la zana....?” Mmalo mwa, chimene akunena...”“gwirizanani nacho chabwino” Awo ndi mafunso olakwikatu.

Nkhani sikuti ndingayandikirane bwanji ndi tchimo opanda kuchimwa. Ndipo kodi ndingayandikire bwanji kwa Mulungu. Kodi ndingakhale bwanji wa chiyero? Chifukwa pamene muli a chiyero, osati angwiwo, chiyero “inu enieni” angathe kuwonekera chifukwa mutha kukhala woona mtima

Ndipo chimodzi mwa zinthu zokumana nazo zimene ndi zamphamvu ndi zofunikira kwambiri zimene mudzakhale nazo mmoyo mwanu ndi kukhala mu gulu la anthu amene ali ndi chitetezo, amene amakondadi inu ndi kuti inu mumawakondadi ndipo “inu weniweni” amaonekera, “Inu weniweni” amene akupita patsogolo kwambiri, “inu weniweni” ndi zonse zokhumudwitsa, ndi zopweteka ndi zolimbana nazo, “inu weniweni” okhala ndi mavuto enieni. Ndipo pamene mukubweretsa zolimbana nazo zanu, simuweruzidwa. Mumakondedwa ndipo “inu weniweni” amene amasowekera chithandizo mumapeza thandizo ndipo, “inu weniweni” amene amsowokera kuyankha, ndipo ngati monga tonse timachitira pa kanthawi kena kudzudzulidwa.

Onani, ili ndi gawo la maziko la mudzi weniweni, ndipo anthu ambiri sanakhalepo nawo. Ndipo choncho timathera kuchita, mmmalo molola Mulungu kutisanthula ife, timatha mphamvu zathu zambiri kuyesetsa kubisa tchimo lathu. Ndiye choncho tikuwononga mphamvu zathu zonse kuyesetsa mwina pakubisa kapena kuthana ndi kulakwa kwathu kapena kuthana ndi thupi lathu kapena kuzimeza ndi chakudya kapena ntchito kapena ndalama kapena kupita ku msika kokagula zinthu kapena kuthamangitsa.

Ndi kotero ngati “inu weniweni” wawonekera, ichi ndi chiyambi cha mudzi weniweni, koma ziposa pamenepo. Umakumana ndi zosowekera zenizeni, osati sachipha maso kapena wokhala wabwino kamodzi. Mudzi weniweni sumangochitika pomwe mukuchita tizinthu ting’onoting’ono tabwino kapena chinthu chabwino chimodzi pano ndipo sizangakutengereni inu mtengo waukulu kwambiri. Mudzi weniweni umachika pomwe “inu weniweni” wawonekera. Dziwani akunena kuti kudzikhuthula – “kudzikhutula kwa wina ndi mnzake mwa chikondi cha pa abale” – kudzichepetsa-“ kupereka chikondi kwa wina ndi mnzake mwa ulemu.

Zosowokera zenizeni kuti zitheke nthawi zonse kumakhudza kudzikhulula ku mbali yathu ndi kudzichepetsa. Mawu akuti “kudzikhutula” panopa ndi a mphamvu. Akunena kuti mukusoweka kudzipereka kwa wina ndi mnzake ndi kupereka miyoyo yanu kwa wina ndi mnzake monga mmene mungachitire ndi abale anu a magazi amodzi. Kwa anthu amene mumamva nawo kuti muli ndi udindo wowaonetsera khalidwe labwino. Ndipo akuti, “mudzikhutule kwa wina ndi mnzake” – bwanji? Mu chikondi cha pa abale. “Philadelphia”, awa ndi mawu ake. Ndi kudzipereka uku ku banja la lachikondi, kukhala pamenepo chifukwa cha wina ndi mnzake, kuchita chilichonse chimene mungachite.

Gawo la mudzi weniweni ndi pomwe inu mwadziyika pachiwopyezo – zomwe zimatchedwa chikhulupiriro – ndipo mmakondana wina ndi mnzake ndipo anthu amapeza chikondi kudzera mwa inu ndiye kenako lye amapereka. Pomwe “inu weniweni” wakumana ndi zosowekera zenizeni kudzera mukudzikhutula ndi kudzera

mukudzichepetsa, chifukwa kumapeto kwa tsiku, mukudziwa chiyani, mumaganizira kwambiri za anthu ena kuposera inu eni ake.

Lembani pambali pa zolembe zanu Afilipi mutu 2, ngati mukufuna, ndime 3 ndi 4. Mtumwi Paulo akunena ndi kuganiza pamene izi zili zokhudza aliyense: “Musacite kanthu monga mwa chotetana kapena monga mwa ulemerero wopanda pake komatu ndi kudzichepetsa mtima, yense ayese anzache omposa iye mwini.” Kodi izi zingasithe bwanji gulu lanu laling’ono, kodi izi zingasithe bwanji banja lanu? Munthu yense asapenyere zache za iye yekha, koma yense apenyerenso za mnzacheyo.” Pamenepo akupitiriza kunena, “Mukhale nawo mtima mkati mwanu umene unalinso mwa Khristu Yesu, ameneyo pokhala nawo maonekedwe a Mulungu, sanachiyesa cholanda kukhala wofanana ndi Mulungu, koma anadzikhutula yekha, natenga maoenekedwe akapolo, nadzichepetsa yekha nakhala womvera kufikira imfa.” Kudzichepetsa. Kudzichepetsa ndi kuyika anthu ena, kuwapatsa zokonda zawo, pamene mukuwakuweza.

Onani pomwe mukuyenda mgulu laling’ono, kapena pomwe mukulowa mu tchalitchi, kapena pomwe muli mbanja mwanu ndi kukhala pa tebulo – chimene ndikuyembekezera kuti mmachita – tonse a ife tili ndi galsi limodi kapena magalasi awiri. Galasi limodzi ndi la amene wandifunsa ine funso, amasamala za ine, chifukwa chiyani wina aliyense sanandikumbatire, zikuthekha bwanji kuti wina aliyense akuwoneka wokondwa kwambiri ndipo palibe akusamala za ine, ndinapita ku gulu laling’ono ndipo palibe anawoneka kuti akundimvetsera pomwe ine ndimamaliza nkhani yanga, ndipo ndili ndekha ndipo ndikusowekera bwenzi ndipo nanga za...ndipo nanga za.... Ndipo awa ndi magalasi amodzi.

Ndipo anthu ena amayenda ndi magalasi amene akuti, ndili ndi zosowekera ndipo Mulungu akudziwa kuti ndi chiyani, koma ndikudabwa kuti Iye akufuna ndani kuti akhale ngalande ya chisomo mu gulu ili laling’ono kapena pomwe ndaweruka ku ntchito kubwerera kunyumba. Ndatoperatu, sindikufuna kukamba za zinthu izo zonse zimene ndadutsamo, koma ndikudziwa mkazi wanga kapena mwamuna wanga kapena ena a ana anga, adzasowekera winawake amene ndi wamoyo ndi wosamalira, ndipo ndikufuna ndipange ndi kupeza mmene ndingawayikire iwo pamwamba pa ine, kodi ndingawapatse bwanji chikondi poyambira.

Ndipo pano pali gawo lodabwitsa. Anthu awo amene amakumana ndi chimwemwe chodabwitsa, ndipo anthu amawawunjikira. Chifukwa Yesu, “Patsani, ndipo kudzapatsidwa kwai nu; muyeso wabwino, wotsendereka, wokuchumuka, wosefukira, anthu adzakupatsani mmanja mwanu, ndi muyeso womwewo muyesa nawo inu...”

Ndipo zitha kuphatikamo ndalama, koma iye samalankhula za ndalama. “Ndi muyeso womwewo muyesa nawo inu, kudzapatsidwa kwai nu; muyeso wabwino, wotsendereka, wokhuchumuka, wosefukira, anthu adzakupatsani mmanja mwanu.” Onani, kumenya khoma la uzimu, pomwe timakhala kakasi kawirikawiri ndi “inu weniweni” sawonekera. Ndipo ngati “inu weniweni” sawonekera – ndipo ngati “inu weniweni” wawonekera kawirikawiri sitikufikira zosowejera zenizeni. Tikungokumana ndi zosowejera zabwino kapena zachiphamaso.

Koma kenako akuti osangoti “inu weniweni” yekha ndi ine tikusowejera kuwonetsera ndi kukumana ndi zosowejera zenizeni, koma iye akuti musowejera kuchichita pa chifukwa cholondola, osati kusangalatsa anthu. Akuti, “Musakhale aulesi mmachitidwe anu; khalani achangu mu mzimu tumikirani Ambuye.” Musakhale “aulesi mmachitidwe” kwenikweni mawu ake ndi “ulesi”. Tanthauzo lake lenileni sikuchita mochedwa.

Kukhalani achangu muuzimu ndi chithunzithunzi cha madzi ochokera muphika umene wayamba kuwira. Ali ndi maganizo awa a pomwe osonyeza kuwira zoonza, atangoyamba kubwata. Mphamvu izi, chilakolako ichi, kuganizira uku, wachangu mu uzimu, osati udindo, ntchito, ndikulingalira kuti ndiyenera kuchita ichi, kuchita ichi ku gulu ili, munthu uyu ali ndi chosowejera, kodi mukuganiza chiyani? Ndikulungalira zakuti timuthandize. Ichi sichinthunzithunzi chimene tili nacho. Ndipo dziwani kuti chilingalira sichimene tidzapeze kapena anthu adzaganiza zabwino za ine. Sindikuchita pang’onopang’ono za chilimbikitso zimene Mulungu amandipatsa. Ndidzadzidwa ndi chidwi chimene chimachokera kwa Mulungu, ndipo ndidzachipanga ngakhale kungopangira iwo koma kumutumikira Iye.

Ndikufuna ndikufunsi funso ndipo ndikufuna inu mukweze dzanja lanu, ndikuganiza kuti mwapulumukanso. Musamangike. Ndikuganiza kuti mukhala bwino. Kodi ndi angati mwa inu amene mwakhala mukuyankhula ndi mnzanu kwambiri kapena kukhala mugulu laling’ono, makamaka lakusanthula Baibulo. ndipo wina wake mu gulu losanthula Baibulo anene kuti, “Hey, nonse mundipempherere ine? Ndine waulesi ndipo ndikusowejera chithandizo cha ulesi wanga.”

Kodi ndingawone manja aja? Ichi ndi chodabwitsa. Onani, anthu ambiri saganizira kuti ndi alesi. Koma gawo lalikulu ndi lakuti tili ndi mawonedwe olakwa a ulesi. Timaganizira kuti ulesi ndi anthu amene amonera TV maora asanu ndi awiri, kusewera maora anayi pa masewera a pa Video, ndi kudya atakhala pa sofa masiku osawerengeka. Ndi alesi.

Tanthauzo la ulesi mu Baibulo silakuti simukuchita chimene ndi chosowokera kuchitika pomwe chikusowejera kuchitidwa. Timaphimba ulesi wathu ndi zinthu zabwino. Mulungu amayankhula mu mtima mwanu ndi Iye amati, “Mikusowejera kupepesa kwa

munthu uyo.” Ndiye kotero mumaganiza, ohoo, eya, ndikuganiza ndidzawerenga mutu mu Baibulo kapena kupemphera.

Lingalirani chiyani? Sichifuniro cha Mulungu kupemphera kapena kuwerenga mutu mu Baibulo pomwe lye akunena, “Pitani kapepeseni kwa munthu uyu.”

Onani, ulesi ukukana kuchita chimene ndi chosowekera kukuchita pomwe chikusowekera kuti chichitidwe. Tili ndi mitundu yonse yamakanidwe ndi mapewedwe. Ndipo akuti, mu zolinga zanu osakhala aulesi. Utumiki weniweni kwa Mulungu umadziwika ndi khama, kupanga bwino kwambiri pa chimene tikuchita ndi mmene tingachitire ndi changu...kukonda kutumikira Mulungu ndi kukonda anthu osati kukondweretsa anthu kapena kusangalatsa anthu.

Tsopano ambiri a ife, tinabwera kwa Khristu kuchokera kumakomo osokonekera. Bambo anga anali chidakwa, munthu wabwino kwambiri, koma sindinadziwe chimene ichi chinatulutsa mpaka nditakula, ndikuwerenga zinthu zonse ndikuzindikira, oooh, ameneyo anali ine ndi awo anali achemwali anga ndipo oooh, anali ovutitsidwa. Ndipo udindo umodzi mubanja la chidakwa ndikubweretsa mtendere ndi kukonza zinthu zowonongeka.

Chabwino nditabwera kwa Khristu, sindinazindikire icho. Zinanditengera ine nthawi kuyamba ndi uzimu, ndipo pomwe ndinayamba chimene ndinapeza, ndinayesetsabe kukonza zinthu zowonongeka ndi kugwira ntchito pa zinthu zanga zosokononekera tsopano mu thupi la Khristu.

Ndipo chimene ndinapeza mu gulu ili la anthu amene amazitcha okha Akhristu, ndipo ndinali wosasandulika kwenikweni ndiye zinthu zazikulu zambiri zimachitika. Koma ndinapeza kuti ngati mwaloweza ndime zambiri, ndipo mmatumikira anthu, ndipo ngati munganene zinthu zolondola ndipo mukhala okonda kuchita mumalandira kuyamikiridwa kwambirri ndi chitsimikizo.

Ndipo kotero poyamba kwa pang'onopang'ono ndinajijirika. Ndinaloweza ndime zochuluka, ndinasanthula Baibulo, ndinali pa gulu ili, ndinatsogolera kusanthula Baibulo, ndinachita ichi ndinangokhala ngati wamisala. Ndinapenga kotero kuti nthawi zina ndinaganiza kuti ndingathe kudwala nazo.

Ndiye ndinali ndi mwayi uwu wopita ku mzinda ndi anthu ena ndi kupeza ntchito. Kunali mwina mwake anthu zala limodzi kapena mazana awiri, ndipo timakhala mutimagulu ta anthu asanu. Timatha kukhala ndi mtsogoleri wagulu ndi anthu anayi ndipo amatha kukuthandizani kukula muuzimu, ndiye mmapeza ntchito ndi kufalitsa uthenga wabwino. Inali ngati nyumba yotentha yokukuliramo muuzimu zinali zopinduladi kwambiri.

Koma pa gulu ili la padera linali ndi njira yowoneka bwino yofikira pa kuyeretsedwa kapena mmene mungakulire mmuzimu. Ndipo njira yawo imaphatikiza mni umunthu wanga wokondera ndi maziko amene anali ngati namondwe wangwiro wopangira a Falisi. Ndiye potero pakutha pa chirimwe chiimenecho ndinaganiza zakuti mukusowekera kuchita ichi panali kusowekera kusanthula Baibulo, kugawana ndi ena za chikhulupiriro, ndipo munsowekera kuchita chimenechi. Pamapeto pache pa kusanthula Baibulo, mumafika kumapeto ndi kukumana ndi mtsogoleri wanu aliyense payekha ndi kukupatsani zowunikira ndi kunena. “Pamene mukubwerera ku Kampasi kwanu, pali chinthu china chake choti muganizire zimene zikuthandizeni kwenikweni kukula muutumiki wanu wa pa Kampasi.”

Ndipo anthu ena amalankhula ndipo anali wokhazikika monga, oooh, ichi chikhoza kukhala chiwopsezo. Ndikuganiza kuti ichi chidzakhala chabwino, chabwino kwambiri. Chifukwa mudziko langa lachinsinsi, ndikuganiza kuti ichi chidzakhala chabwino kwambiri, ndikuganiza kuti ndine wodziletsa kwambiri kuposera wina aliyense pano. Ngati akadapereka mphotho ya Mkhristu amene ndi wochita bwino paliponse, wa phindu kwambiri ndikadakhala mwina mwake ineyo.

Kotero ndimayenera kukhala ndi msonkhano ndi John mtsogoleri wa gulu limene ndili, ndipo zoonadi ndinaona kuchedwa kudikirira. Ndikuganiza kuti mapeto ake ndinalandira chizindikiritso chenicheni chimene ndinayenera kulandira. Ndipo mwina mwake akadandiwuza kuti ndidzakhala ndi zokhudza mosuntha anthu kwambiri. Ndipo John anali wofatsa. Anali mtsogoleri wag ulu limene ndili.ga ndipo anali mtsogoleri amene anali ndi njira ya utsogoleri. Moonadi ndimadikira kutsogolo kwa msonkhano ndipo mwachinsinsi ndinayembekezera kuti anali atawona kudziletsa ndi chimene ndinachita ngati chitsanzo cha nthumwi zina za mugulumo, moyo wautumiki umene ndinali nditasonyeza mmaubale athu, ndipo chidziwitso ndi chikhulupiriro chimene mothamanga chinakula mmoyo mwanga. Ndinali nditagwira ntchito molimbika ndipo ndinali wokonzekera kulandira chovomerezedwacho.

Koma msonkhano wathu sunayende monga mmene ndinayembekezera. Ngakhale ndinali wodzadzaza ndi changu ndipo ndinachita bwino mu chirimwe chonse, chiwunikiro cha John pa ine chinandidabwitsa ine ndi mmene anawunikira za moyo wanga wauzimu. Kunali kusiyananiratu ndi kwa ine mwini wake. Ndi mawu ochepa okha, ananena kuti akundiyamikira kudziwana nane mu nthawi yonse ya chirimwe ndi kuti Mulungu anavumbulutsa ndime zitatu mmumtima mwake zimene anafuna kugawana nane. Anandipatsa makadi a zolembamo ndi kunena kuti, “Ndikupempherera kuti Mulungu akuyankhuleni pamene mukubwerera ku Kampasi kwanu.” Kusweka mtima.

Kotero ndinalandira izi zitatu, khadi ya mutatu muufupi ndi musanu kutalika kwake yokhala ndi zimene zinalembedwa pamanja. Yoyamba inati, “Pakuti kodi ndikopa anthu tsopano, kapena Mulungu? Kapena kodi ndifuna kukondweretsa anthu? Ndikadakhala wokondweretsabe anthu, sindikadakhala kapolo wa Khristu.” Agalatiya 1:10. Ndipo ndinaganizira kuti, hmmm, ndime iyi inali yosangalatsa.

Ndime yachiwiri, Yohane 5:44 “Mungathe inu bwanji kukhulupirira, popeza mulandira ulemu wina kwa mnzache ndipo ulemu wakuchokera kwa Mulungu yekha simuufuna?” Mwina mwake pali uthenga pano. Chikaiko chonse chinachotsedwa ndi ndime yachitatu, Luka 16:15 “Ndipo anati kwa iwo, Inu ndinu odziyesera nokha olungama pamaso pa anthu; Koma Mulungu azindikira mitima yanu; chifukwa ichi chimene chikuzika mwa anthu chiri chonyansa pamaso pa Mulungu.”

Onani, “inu weniweni” angathe kuwonekera ndipo angathe kukumana ndi zosowekeka zenizeni ndi mungathe kuchita potumikira inu, monga mmene ndinachitira kupeza chitsimikizo, kusewera sewero mkati mwa mudzi wa Akhristu kumene mumawonekeka ngati ndinu wokonda. Koma chenicheni chimene mumachita ndi kumaliza ndi kugwiritsa ntchito ndime zonse zimene mukudziwa ndi ntchito zonse zabwino zimene muli nazo kutenga dziko lanu laling’ono lomwe mumangotumiza fanizo losiyana la munthu amene ndi wonamizira ndi wabodza amene mukukonza kulephera kwa inu eni kuti mupeze anthu amene angakuvomerezeni mmalo monena, “Ndine wovomerezedwa mwa Yesu.”

Ndipo mayeso enieni a zolinga zanu nthawi zonse pomwe mwatengedwa ngati wa ntchito pomwe wina aliyense sakuzindikira, pomwe sakunena zikomo, pomwe mwayamikiridwa, pomwe mukumva ngati munthu mmodzi yekha amene akuwona zimene ndikuchita ndi Mulungu.

Ndipo mkati mwa mtima wa mitima yanu, ngati munganene, “Eya, ndithu, ichi ndi cholondola, ndikutumikira gulu la mmodzi.” Zoyankha za anthu ndi chitsimikizo cha anthu....”Mulungu, pomwe chabwera kapena sichikubwera, chimenecho sichifukwa chimene ndikuchitira.” Ndi “inu weniweni” kukumana ndi zosowekeka zenizeni pa chifukwa cholondola.

Ndipo pomaliza, ndi njira yolondola. Mudzi weniweni nthawi zonse udzaseweretsedwa mkati mwa zowawa ndi zovuta ndi zopomboneza. Mu dziko lakugwa ndi kovutadi kwenikweni kukhala ndi nthawi ya mudzi weniweni. Ndi kovutadi kwambiri kukhala moona mtima pomwe mwaphulitsidwa.

Ndiye kotero njira yolondola siili mu mphamvu za inu eni nokha, osati muchimene mungachite, osati mumphamvu ya umunthu wanu, osati ngati kuti Yesu ndi wina wake weniweni wongomutsatira, “ Ndigwira ntchito molimbikira ndipo ndingathe kukonda anthu ndipo nditha kukhala weniweni ndipo ndingathe kuchita ichi ndi izi ndi ndalama zimene ndili nazo. Ayi, ayi, ayi. Akunena kuti njira yolondola – ndi kulunjika kowona patsogolo ndiponso kulunjika kowona kunja. Ndipo likuti musangalale muchiyembekezo. Awa ndi maganizidwe. osati kusangalala mu zochitika kapena zoyankha za anthu.

Akuti, mukusowekera kuchita chiyani? Kulimbika mmasautso. Mmawu ena, mkati mwa pomwe pali zovuta, mumakana kusiya chifukwa mukhala moyo ndi gulu ili la anthu, ndipo ndi kovuta ndipo chilichonse mwa inu chikufuna kusiya, koma mmakana. Ndipo mudzathandizira anthu kuti achikwaniritse. Ndipo chida chanu chidzakhala kudzipereka ku pemphero. mukhala ndi kugawana kwa nthawi ndi kuti ... “Sindikudziwa kuti ndalama zolipirira nyumba zichokera kuti, sindikudziwa kuti vuto ili ndithana nalo bwanji, sindikudziwa mmene ndingathanirane ndi vuto ili mbanja mwanga, sindikudziwa kuti chizolowezi ichi choipa chovuta kusiya ndingathane nacho bwanji. Koma Mulungu ndikukupemphani chithandizo, ndipo ndidzayamba kugawa moyo wanga moonekera, moonadi ndi gulu la anthu amene ali otetezedwa ndipo tiyenda mu izi pamodzi.”

Ndiye pali kulunjika kowona patsogolo. Sikuthekera kwa zida zanu. Mzimu amene anadzutsa Yesu kuchokera kwa akufa amakhala mwa mwana aliyense wa Mulungu. Muli ndi mphamvu zonse zimene mudzadzisowekera, koma mphamvu zimenezo zimapezeka kudzera mu Mawu Ake ndi kudzera mmudzi wa anthu a Mulungu, ndiye mphamvu imeneyo imapezeka mukayamba kupemphera.

Chimodzi cha maumboni akulu a kudzichepetsa kwenikweni ndi kudalira pa moyo wanu wa pemphero. Ndipo ine ndakhalapo pamenepo pomwe moyo wanu mosakayika umakhala ngati mukudzuka, mukutenga kapu ya khofi, mukulowa mu galimoto mwanu, mukuthamanga, mukupita, kuli msokhano waukulu, mukufunika kuchita izi ndi ana anu, mukufunika kupanga chiganizo chachikulu, ndiye mukuchita zonse izo, ndiye simuli pa mawondo anu kunena kuti, “Mulungu sindikudziwa chimene ndichite; Mulungu ndiliba nzeru. Mulungu, sindikudziwa mmene ndingachitire ichi ndi mmodzi mwa ana anga; Mulungu ndikusowekera... chonde.

Pomwe simukuchita izo, chimene mukunena kwa Mulungu ndi, “Ndikudziwa Munalenga dziko lapansi. Ndikudziwa ndinu a nzeru zonse, ndikudziwa Mukudziwa chilichonse chimene chikuchitika lero, mawa mpaka kalekale, koma sindikusowekera thandizo lotero.” Ndikuganiza kuti ili ndi tanthauzo la kudzikuza, sichoncho? Moyo wathu wopanda pemphero mosakaika umanena kuti, “Ndapeza ichi. Mudzingosunga, dziko likuzungulira. Izi ndingathe kuthana nacho.” Ndipo Mulungu amadana ndi munthu

onyada ndi kupereka chisomo kwa odzichepetsa. Uku ndikutenga kuchoka pa zida Zake zodabwitsa.

Ndiye kutero pali kulunjika kowona patsogolo, ndiye kenako kukutsatidwa ndi kulunjika kowona kunja. Dziwani chimene ikunena. Ikunena kuti, “Patsani zosowa oyera mtima, cherezani aulendo.” Ndi pamene akunena kuti kuli kulunjika kowona kunja. Ndiye pali nthawi zimene Mulungu adzakufunseni kuti musonkhe.

Tanthauzo lenileni la kusonkha ndi kupereka ndalama kwa anthu osowa, kupereka nthawi, kupatsa zinthu kwa winawake amene alibe chimene inu muli nacho kwa abale kapena alongo mwa Khritsu, kusonkha ku zosowa za okhulupirira oyera mtima anzathu. Ndipo pomwe mwachita izi, kuli ngati, nanga bwanji kwa ine? Mulungu akuti; “Zimenezo ndazikonza kale.

Ndiye kenako akuti “chezerani alend.” Kwenikweni mawu akuti, “chezerani osawadziwa.” Onani, mungathe kukhala mu mudzi weniweni. Ndikuganizira kuti izi zaphatikizidwa kumapeto zedii pa chifukwa chofunikira kwambiri. Tingathe kukhala ife anayi kapena osakhalaponso. Timakhala ndi kusanthula Baibulo kwakulu, ndife oyandikana, ndifedi enieni, ndife omasuka, tingathe kugawa chilichonse, ndife othandiza moposa, takhala tikuchita zimenezi kwa ife tokha kwa zaka 25. Eya, zabwino kwa inu ndikudabwa ngati palinso wina wake mu tchalitchi amene akanatha kusowekera izi muzaka 24 kapena 25 zapitazo.

Kodi anthu amene sakondedwa ndi ndani? Kodi anthu amene ali wokhawokha ndi ndani? Kodi ndi anthu ati amene polowa muno, mungathe kunena kuchokera mmaonekedwe a thupi lawo kuti akhala akudutsa mu zovuta mu sabata imeneyi? Kodi ndi anthu ati, amene pomwe tikamaliza, ndipo akutuluka, mungathe kuwona maso awo ndi onyezimira pango’no ndi owoneka madzi chifukwa Mulungu akuchita china chake mmitima yawo? Kodi ndi anthu ati amene akusowekera inu kuti muwatsate ndi kuwatsegulira khomo lanu ndi kuwayitanira iwo ku chakudya? Kodi ndi anthu ati amene amasowekera inu kuti mukhale mukupezeka kwa Yesu?

Onani, ichi ndi chimene chimaboola tsindwi. Umu ndi mmene mumamatakatira mbewu za Mawu a Mulungu mumtima wabwino ndi wowona ndi nthaka. Mmalo mwa mudzi weniweni, “inu weniweni” kukumana ndi zosowekera zenizeni pa chifukwa cholondola munjira yolondola ndi kumene kusanthulika kozizilitsa kumachitika.

Zinali zomukhudza zedi Yesu. Dziwani mmene anatsekera pemphero lake lomaliza limene linalembedwa mmalembo. Akunena kuti. “koma sindipempherera kwa iwo okha,” ophunzira ake. “Komanso iwo akukhulupirira Ine chifukwa cha mau awo,” kunena kuti, “onse akakhale amodzi, Atate, monga inu Atate mwa Ine, ndi Ine mwa Inu kuti iwonso akakhale mwa lfe.”

Umodzi wa Atatu uli mudzi weniweni. Ndipo Yesu akakupemphera kwa Atate kuti timve ndi kuchita zimene Iwo Amachita. Ndiye kenako yang'anani pa mawu a cholinga, "kotero kuti." Ichi ndi chifukwa chimene ichi chili chofunikira kwambiri, "Kotero kuti iwo akakhulupirire kwa inu Munandituma ine"

Chinthu chosachititsa chisoni kwambiri pa maso pa dziko lapansi ndi pomwe inu mwakonda moonadi, alongo ndi abale ndi "inu enieni" kukumana ndi zosowekera zenizeni pa chifukwa cholondola munjira yolondola.... iwo amene ali kunja kwa Khristu adzamvetsa ndi kukhulupirira kuti Yesu angathe kukhala Mpulumutsi wawonso.